NYA_TTB_0938_20161102**_script**

Danieli : 9:20-27

Mutu : Ulosi wamasabata makumi asanu ndi awiri

Ndipereka moni wa Kumwamba kwa inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero tiyamba ndi mau a Mulungu opezeka pa Ahebri 4:16, amene akuti, “Potero tilimbike mtima poyandikira mpando wachifumu wachisomo, kuti tilandirechifundo ndi kupeza chisomo chakutithandiza nthawi yakusowa.”

Mupologalamu yatha timakambirana pa Danieli 9:1-19, za pemphero la Danieli lokhudza Israyeli. Ndipo lero pa Danieli 9:20-27, tisanthula ulosi wamasabata makumi asanu ndi awiri.

Danieli 9

Mupologalamu yatha tidalekeza ndi Danieli akupempha Mulungu kuti akhululukire Israeli chifukwa cha dzina lake loyera ndi kulungama kwake kudzera m’chisomo cha imfa ya Yesu Kristu, momwe adaperekadipo la machimo athu onse.

Ndiye ndikoyenera kudziwa kuti pamene Danieli anali kupemphera ndiye kuti yankho linali kubwera nthawi yomweyo.

20. Ndipo pakunena ine ndi kupemphera, ndi kubvomereza tchimo langa ndi tchimo la anthu a mtundu wanga Israyeli, ndi kutulachipembedzero changa pamaso pa Yehova Mulungu wanga, chifukwa cha phiri lopatulika la Mulungu wanga.
21. Inde pakunena ine m'kupemphera, munthu uja Gabrieli, amene ndidamuonam'masomphenya poyamba paja, anaulukamwaliwironandikhudza ngati nthawi yakupereka nsembe ya madzulo.

Nkhani ili mundime iyi, ikuti pamene Danieli anali kupemphera, yankho la pemphero lake linatumizidwa nthawi yomweyo. Kutsimikiza kuti yankho linaperekedwa kale ngakhale Danieli anali asanatsirize kupempha.Izi, zinachitika chifukwa cha lonjezo la Mulungu pa Yesaya 30:19, pamene adanena kuti, "Pakuti anthu adzakhala m'Zioni pa Yerusalemu; iwe sudzaliranso, Iye ndithu adzakukomera mtima pakumveka kupfuula kwako; pakumva Iye adzayankha." Komanso pa Yesaya 65:24, akutsindika kuti, "Ndipo padzakhala kuti iwoasanaitane, Ine ndidzayankha; ndipo ali chikhalire, Ine ndidzamva."Danieli akunena kuti pamene iye

akalichigwadirepamaondo wake, komanso akanali ndi zina zofuna kupempha, yankho linali kudza kwa iye. Ichi, ndichimene akunena pa verse 21, pamene akuti, “Inde pakunena ine m’kupemphera, munthu uja Gabrieli, amene ndidamuonam’masompenya poyamba paja, anaulukamwaliwironandikhudza ngati nthawi yakupereka nsembe ya madzulo.”

Tsono Danieli mupemphero lake akutchula zinthu ziwiri zikulu-zikulu. Poyamba akugonja chifukwa cha uchimo wake ndi uchimowa mtundu wa anthu ake, Israyeli. Tamvani akunena kuti, “Ine ndikupemphera ndi kubvomereza tchimo langa ndi tchimo la anthu a mtundu wanga, Israeli.” Tsono taonani kuti Danieli ndiye anali munthu wabwino ndi wolungama, koma akupezabe tchimo m’moyo mwake lomwe tsopano ali wokonzeka kubvomereza pamaso pa Mulungu. Kutsimikiza kuti palibedi munthu wolungama padziko lapansi, ndipo kuti sachitatchimo. Monga mwa mau amene adanena Paulo pa Aroma 3:23, pamene adati, “Pakuti onse anachimwa, naperewerapaulemererowa Mulungu.” Tere, ndichifukwa chake Yohane m’Kalata yake pa 1 Yohane 1:8, adadziikamgulu la anthu ochimwa pamene adanenetsa kuti, “Tikati

kuti tiribe uchimo, tidzinyenga tokha, ndipo mwa ife mulibe choonadi."

Tsono Danieli mundime imeneyi, akubvomereza kuti ndiye wochimwa. Ndiye chochititsa chidwi ndichakuti m'Baibulo palibe penapaliponse pamene Danieli anapezeka wochimwa. Ngakhale adani ake omwe anabvomereza kuti sangamupezerecholakwa.Kodi tinene kuti Danieli anali kunama pamene anabvomereza tchimo lake pamaso pa Mulungu?Yankho likuti ayi, sadaname, koma kuti adali ndi chidziwitso cha mau aja tawerenga kale, akuti anthu onse anachimwa. Mwanjira ina tikutsimikiza kuti Danieli anali wochimwa ndipo kuti lamulo silingathe kupulumutsa munthu. Ichi, ndichifukwa chake Danieli anali kungodzipereka yekha pamodzi ndi anthu a mtundu wake ku chifundo cha Mulungu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna tiphunzire kuti anthu abwino ndiwo amene amayesetsa kupepuza nkhawa zawo pakudzipereka pamaso pa Ambuye, mwakubvomereza machimo awo. Komanso tikunena kuti chifukwa cha ulemerero wa Mulungu, iwo amene amakhudzidwa, ndi moyo wa mpingo wawo, miyoyo ya anthu anzawo, nthawi zonse amalirira kwa Ambuye, chifukwa cha

zochimwa za ena. Kodi inu mumakhudzidwa motani ndi moyo wa ena?

Kachiwiri tikuona Danieli akupembedzera Israeli chifukwa cha chionongeko cha Kachisi wa Mulungu. Chinthu ichi, ndichimene chinamufikiraDanieli koyambirira kusiyana ndi zinthu zina mongazothandiza moyo wakunjawa munthu. Apa, anadzikhuthula kwambiri mukupempha kwake.Pachifukwa chimenechi, Mulungu anatuma mngelo wake ndi yankho labwino.Kutsimikiza kuti Mulungu amakondwera ndi pemphero lamoyo. Ndiye ndikofunika kudziwa kuti pamene tipempheramodzipereka, pachinthu chimene Mulungu analonjeza kuchita, ife ndichikhulupirirotimakhala kuti talandira kale yankho lake.

22. Ndipo anandilangiza ine, ndi kulankhula nane, nati, Danieli iwe, ndaturuka tsopano ine kukuzindikiritsamwaluntha.
23. Pakuyamba iwemapembedzero ako, linaturuka lamulo; ndipo ndadza ine kukufotokonzera; pakuti ukondedwa kwambiri; zindikira tsono mau awa, nulingirire masomphenyawo.

Danieli akunena kuti mngelo Gabrieli anamuuza iye za chifuniro cha Mulungu, kuti afuna kubwezeretsa a Yuda kudziko la kwawo,

kukamanganso mzinda wa Yerusalemu, Kachisi wa Mulungu ndi kubwera kwa Mesiya. Tsono yankho ili, ndilomwe linadza pamene Danieli anali asanathe kupereka pembedzero lake kwa Mulungu. Uku, kunali kukwaniritsa mau aja tinawerenga kale apa Yesaya 65:24, amene akuti, “Ndipo padzakhala kuti iwo asanaitane, Ine, ndidzayankha; ndipo ali chilankhulire, Ine ndidzamva.”

Tsono chinthu chomwechaonekachi, chingotsimikiza kuti Danieli anali kukondedwa m’Mwamba. Awa, ndiwo mau amene adanena Paulo pa Aefeso 1:6, pamene anati, “Kuti uyamikidwe ulemerero wa chisomo chake, chimene anatichitira ife kwaufulu mwa Wokondedwayo.” Kutanthauza kuti inu ndi ine, ngati wokhulupirira ndife wokondedwa m’Mwamba popezatibvomerezeka pamaso pa Mulungu chifukwa cha Wokondedwayo (Kristu).

24. Masabata makumi asanu ndi awiri alamulidwira anthu wopatulika, kumarizacholakwacho, ndi kutsiriza machimo ndi kutetezera mphulupulu ndi kufikitsa chilungamo chosalekeza ndi kukhomera chizindikiro masomphenya ndi zonenera, ndi kudzoza malo opatulikitsa.

Pano ndifuna kuyamba ndi mau akuti, ukapolo wa ku Babulo wa a Yuda ndicho chiyambi cha kusintha kwa zinthu m'mbiri ya Ufumu wa Mulungu. Tikunena kuti Danieli amene anamvetsetsa ulosi wamasabata makumi asanu ndi awiri kudzera m'buku la mneneri Yeremiya za kutha kwa ukapolo wa zaka makumi asanu ndi awiri, akufotokonzerakumpingo za kumasulidwa kwina komwe kudzakhalakwamuyaya. Kutanthauza kuti pakutha kwa zaka makumi asanu ndi awiri za ukapolo, pakubweransokumasulidwa kwina kwa masabata,azaka. Tsono Danieli analandira kumasulira kumeneku ngati yankho la pemphero lake. Taonani Danieli anapemphera za kumasulidwakwa anthu a mtundu wake ndi kumangidwa kwa Mzinda woyera wa Yerusalemu. Koma taonani Mulungu akupereka yankho lomwe ndiloposa zomwe anali kufunsa komanso kuganizira.

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani iyi, ikuti Mulungu samangoperekazokhazo zomwezapemphedwanso, koma amaonjezerapazokhumba za iwo amene akumuopa Iye. Ichi, ndicho chimene Masalmo 21:4, akunena pamene akuti, "Anakupemphani

moyo, mwampatsa iye; mwamtalikitsira masiku, ku nthawi za nthawi."

Tsono ulosi uwu, ukunena kuti masabata makumi asanu ndi awiri, ayenera kuchulukitsidwa ndi zaka zisanu ndi ziwiri kuti tipezekutalikakwa nthawi momwe zinthu zina zikulu-zikulu zokhudza anthu a mtundu wa Israyeli ndi mzinda wa Yerusalemu zinachitika. Tere, zaka zonsezi zikufotokonzedwa ndi kuchuluka kwamasabatawa. Kutanthauza kuti nthawi iyi inakhazikitsidwa, koma inagawidwam'magawo magawo ndi cholinga chofuna kukwaniritsa zinthu zina zokhudza kukonzanso mzinda wa Yerusalemu ndi a Yuda kupitiliza kukhala anthu a Mulungu, kubwera kwa Mesiya kwa iwo, kupeza madalitso auzimu kwa anthu onse a Mulungu, omwe Danieli anali kukhalanawo. Pachifukwa chimenechi, pamene tikamba za ulosi wamasabata makumi asanu ndi awiri, sitikukamba za masabata okhudza masiku ayi, popeza tikatero ndiye kuti zinthu zonse tatchulazi, sizingakwanamo. Mwanjira ina tikunenetsa kuti masabata makumi asanu ndi awiri, akuimira nthawi ya zaka mazana anayi mphambu makumi asanu ndi anayi (490 years). Ndiye zaka izi, zikugawidwam'magawo atatu

amene ndi zaka zisanu ndi ziwiri (7 years), zaka makumi asanu ndi limodzi ndi awiri (62 years) ndi gawo la chaka chimodzi.

Tsono poyamba akuonetsa zinthu zokhudza moyo wauzimu kuti ndizimene zinachitika m'nthawi yonseyi popeza ndizo ziri zofunika kwambiri.

Chinthu choyamba chofunika kwambiri kuchitika ndicho "Kumarizacholakwacho." Pano Danieli sakukamba za uchimo womwe adachimwa Adamu, ngakhale kuti udachotsedwa ndi Kristu kwa anthu ochepa, komanso sakunena za kuchotsa uchimo wa munthu pa iye yekha ayi, koma kuchotsa uchimo wa mtundu wake, umene unaikidwanso pa iye popeza anatengedwanawo pamodzi ku ukapolo ku Babulo.

Ndiye Danieli anali kuona kumalizikakwa ukapolo wawo wa zaka makumi asanu ndi awiri (70 years) kuti chinali chilango chokwanira, koma chilango chimenechi, sichidaperekedipo ku machimo ya anthu, koma dipo lomwe lidzaperekedwa ndi Mesiya patapitamasabata makumi asanu ndi awiri a zaka (490 years).

Tsono ndifuna muone kuti pamene tikamba zaka 70, za ukapolo ku Babulo, kuchoka ku dziko lawo, ndiye pano ukapolo watha ndipo akubwezeretsedwa ku dziko lawo nakakhalamo kwa zaka mazana anayi, mphambu makumi asanu ndi anayi (490 years), zikutsimikiza kuti, kuchitira chifundo ana ake, koposa kuwalanga, ndicho chinthu chapamtima pa Mulungu.

Kachiwiri, Danieli akunena za “Kutsiriza machimo.”Apa, anali kunena zakutha kwa uchimo wa mtundu wa Israyeli pakubwera kwa Kristu kachiwiri. Tere njira yochotseramachimo ndiyo kupereka nsembe, imene iliKristu, yomwe ndi nsembe yokwanira, kotero kuti onse amene machimo awo anaperekedwa m’nsembe imeneyi, sawerengedwanso ochimwa ndipo palibe chilango chimene chingapatsidwe kwa iwowa. Tere ichi, ndicho chimene Paulo anali kunena pa Aroma 8:1, pamene anati, “Chifukwa chake tsopano iwo akukhala mwa Kristu Yesu alibe kutsutsidwa.” Kutsimikiza kuti pamene inu mukhala mwa Kristu, muli wotetezedwakuuchimo uliwonse.Ili, ndilo tanthauzo la mau akuti, monga momwe Kristu anena kuti zinthu zomwe zimabisikazikwiriridwa, momwemonso uchimo umakhululukidwanukwiriridwa.Ichi, ndichimene

chidamukhutsa Davide pa Masalmo 32:1, pamene adati, “Wodala munthuyowokhululukidwa tchimo lake; wokwiridwa choipa chake.”

Kachitatu tiona mau akuti, “Kutetezera mphulupulu.”Nkhani iyi ikuti pamene a Yuda adzabwezeretsedwa kwawo, kudzakhala kukhululukira mphulupulu yawo. Koma kukhululukira uku, kunali kuimira kuperekedwa nsembe kwa Ambuye wathu Yesu Kristu. Kunena kuti kuzunzika ndi kuphedwakwa Ambuye Yesu, ndiko kunakwaniritsa chilamulo ndi chilungamo cha Mulungu mwa kupereka dipo la uchimo wonse wa munthu. Ichi, ndicho chinali cholinga cheni-cheni cha kudzipereka kwaKristu monga mau apa Ahebri 2:17, akutsimikiza kuti, “Potero kudamuyenera kufanizidwa ndi abale m’zonse, kuti akadzakhalamkulu wa ansembe wachifundo ndi wokhulupirika m’zinthu za kwa Mulungu, kuti apereke dipo la zoipa za anthu.”

Tsono pamene akunena za “kukhomera chizindikiro masomphenya ndi zonenera,” akukamba za kukwanitsidwa kwa masomphenya. Nkhani ikunena kuti ulosi unakhomera chizindikiro mwa Kristu. Kutanthauza kuti ulosi wonse m’Chipangano Chakale, umene unali kunena zaKristu, monga kubadwa kwake, umunthu wake, utumiki

wake, nthawi ndi malo ndi zonse zokhudza chipulumutso cha munthu, zinakwaniritsidwa mwa Iye. Kunena kuti aneneri onse anali kunenera za Kristu, yemwendimneneri Wamkulu woposa onsewo.

Tsono atatha kunena za kumasulidwakwa a Yuda ndi kuperekedwa nsembe kwa Kristu ngati dipo la machimo athu lokwanira, akunenanso za "kudzodza kwa malo opatulikitsa."Apa, sakutanthauza za kudzodza kwa malo a kachisi weni-weni ayi, koma za kupezeka kapena kulowa kwaMesiya m'Kachisi ndiko kungapangitsekupatulika kwa malowo. Kunena kuti monga mau a Mulungu anena kuti wokhulupirira ndiwo Kachisi wa Mulungu, akutsimikiza kuti wokhulupirirayu amakhala wopatulikitsa pamene Kristu akhala mwa iye.

25. Dziwa tsono, nuzindikire kuti kuyambira kuturuka lamulo lakukonzanso, ndi kumanga Yerusalemu, kufikira wodzozedwayo, ndiye kalonga, kudzakhalamasabata asanu ndi awiri; ndi masabata makumi asanu ndi limodzi mphambu awiri, makwalala ndi chembazidzamangidwanso, koma mu nthawi za mabvuto.

26. Ndipo atapitamasabata makumi asanu ndi limodzi mphamvu awiri wodzozedwayoadzalinkhidwa, nadzakhala wopanda kanthu; ndi anthu a kalongawakudzayo adzaononga mudzi ndi malo opatulika; ndi kutsiriza kwake kudzakhala kwa chigumula, ndi kufikira chimariziro kudzakhala nkhondo; chipasukochalembedweratu.
27. Ndipo iye adzapanganachipanganocholimba ndi ambiri sabata limodzi; ndi pakati pa sabata adzaleketsa nsembe yophera ndi nsembe yaufa; ndi paphiko la zonyasapadzafika wina wakupasula, kufikira chimariziro cholembedweratu, mkwiyo udzatsanulidwa pa wopasulayo.

Nkhani ili mundime ino, ikuti Danieli ayenera kudziwa zambiri za bvumbulutso la masabata makumi asanu ndi awiri, ndi asanu ndi awiri. Tsono nthawi yomwe lamulo lomasulira a Yuda omwe anali kuukapolo ku Babulo ndi kumangansokwa Kachisi, ndiyo ikubvuta popeza anthu ambiri akunena nthawi zosiyana-siyana. Ndiye ngakhale lamulo limeneli ndi loperekedwa ndi munthu, koma likugwiritsidwa ntchito pakukwaniritsa chifuniro cha Mulungu. Tsono ngakhale anthu olemba ambiri akusiyana panthawiyi, koma

akugwirizanabe kuti Koresi, ndiye amene pa Ezra 1:1, akulamula kuti a Yuda onse amasulidwenabwerere kwawo ndi kukamanga mzinda wa Yerusalemu monga akunena Yesaya 44:28, kuti, “Ndikunena za Koresi, Iye ndiye mbusa wanga, ndipo adzachita zofuna zanga zonse; ndi kunena za Yerusalemu, adzamangidwa; ndi kwa Kachisi, maziko ako adzaikidwa.”

Tsono tikunena kuti ngakhale pali kusiyana kwa maganizo ya anthuwa, koma lamulo limeneli ndilo likkuuza chiyembekezo cha anthuwa. Tikunena kuti ngakhale m’mbuyomo munali ulosi wa kubwera kwa Mesiya, koma sunakhalepo wokhazikika monga uwu. Kunena kuti mwa ulosi uwu, anthu anali ndi chithunzi cheni-chenichakudza kwake. Izi, ndizo zinaoneka pakudza kwa Kristu pa Luka 2:25, pamene akuti, “Ndipo onani, m’Yerusalemu munali munthu uyu, wolungama mtima ndi wopemphera, analikulindiramatonthozedwe a Israyeli. Ndipo Mzimu Woyera anali pa iye.” Tsono kudzera mwa mau amenewa, tikutsimikiza za kubwera kwa Mesiya, amene ndi Kristu, yemwe anadza panthawi yoikika.

Wokondedwa anzanga apaulendo tikunena kuti lamulo ili, lidzakwanitsidwa ngakhale pakhale nthawi yowawa, koma ichi chidzachitika basi. Kutsindika kunena kuti pamene tiri m'dziko lino lapansi, tiyenera kukumana ndi masautso ndithu.Tere, kukondwa kwathu kuyenera kukhala konthunthumira.

Nkhani ikuti, pamene a Yuda adzabwerera kwawo, ayembekeze kukumana ndi masautso ndithu. Koma chinthu chodziwikakomansochothunzitsa mtima ndi chakuti Mulungu adzapitiliza ntchito yake, monga kumanganso ndi kukongoletsa mzinda wa Yerusalemu ngakhale pakati pa msautso.

Pano titsirize ndi amau akuti a Yuda osakhulupirira, anali kuyembekeza kuti Mesiya akubwera kudzawalanditsa m'dzanja la Aroma, nadzawapatsa mphamvu ndi chuma.Koma pano akuuzidwa kuti Mesiya adzakwaniritsa cholinga china, osati zimene anali kuganiza ayi. Ambuye Yesu, yemwe ndi Mesiya, anadza kudzapereka moyo wachilungamo ndi wachiyero, popeza tonsefetinachimwa ndi kuperewerapaulemererowa Mulungu.

Lero tilekeza pano. Ndiye tinali kukambirana paDanieli 9:20-27, momwe timasanthula za ulosi wamasabata makumi asanu ndi awiri.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!